

# Zifukwa Zimene Ena Sabwera Kwa Khristu

## Za Mkatimu

1. Chifukwa choyamba ndi kuti simukudziwa kuti mukusowa Khristu kwambiri m'moyo mwanu..5
  - a. Umboni wam'Baibulo .....5
  - b. Umboni wa chikumbumtima chanu.....6
2. Chifukwa chachiwiri chingakhale kuti simulapa pamene Yesu ali kukutsutsani ndi mau ake.....7
3. Chifukwa chachitatu chingakhale chakuti simukhulupirira malonjezo a Yesu.....11
4. Chifukwa chachinayi chingakhale chakuti mukuyembekeza kuti mudzalandira bvumbulutso loonjezera kuchokera kwa Khristu.....14

Womasulira mu Chichewa: Jim Kalenga

Akonzi: Maxwell Mandevu, Michael C. Munthali,  
Nathaniel Maxson

© Copyright 2009 Chapel Library.

Permission is expressly granted to reproduce this material  
by any means, provided that

- 1) you do not charge beyond a nominal sum for cost of  
duplication
- 2) this copyright notice and all the text on this page are  
included.

Mukafuna mabuku ena a Chikhristu, tilembereni kalata  
kapena kutiyimbira foni:

**Christian Faith Bookstore**

PO Box 30610

Chichiri, Blantyre 3, Malawi

+265 993 436 951 • christianbooksinfo@gmail.com

In Malawi, contact us for additional copies of this booklet or  
other Christ-centered materials. Please write also for a sub-  
scription to the *Free Grace Broadcaster* (in English).

**Christian Faith Bookstore**

PO Box 30610, Chichiri, Blantyre 3, Malawi

+265 993 436 951 • christianbooksinfo@gmail.com

# Zifukwa Zimene Ena Sabwera Kwa Khristu

Ku Yerusalemu linali tsiku la phwando lalikulu la Chiyuda, kotero kuti mzinda wonse unali wounjikana m'makwalala, kumasangalalira limodzi. Koma pa thamanda la Betesda, Mphunzitsi wina wake, wooneka wachinyamata amene anachokera ku Galileya, anadabwitsa anthu onse pamene anachiritsa munthu wopuwala kwa zaka 38! Koma m'malo mokondwerera, akuluakulu a Chiyuda choyamba anatsutsa wochiritsidwayo chifukwa cha kunyamula mphasa yake pa tsiku la Sabata. Ayuda amaona ngati munthuyu anali kuphwanya lamulo la Mulungu loletsa ntchito iliyonse pa tsiku la Sabata. Analimbananso ndi Mphunzitsiyu, Yesu, chifukwa cha "ntchito" yake ya kuchiritsa pa Sabata! Mu bukhu la Yohane, mutu wake wa 5, tiona m'mene Yesu anawayankhira mwachidule kuti, "Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, Inenso ndigwira ntchito." Mau amenewa Ayuda amawaona ngati kuti Yesu "anadziika Yekha kuti ali wofanana ndi Mulungu." Yohane 5:18.

Pamene Yesu ananena poyera zakuti Iye amafanana ndi Atate anautsa maganizo akupha m'mitima ya atsogoleri a Chiyuda, komabe Yesu anatsimikiza kulakalaka kwa mtima wake pa iwo pamene analengeza pa ndime 34 kuti, "koma ndinena izi kuti inu mukapululumutsidwe." Koma popeza kuti iwo sakanatha kupulumutsidwa koma pokhapokha atam'khulupirira Iye, komanso sakanatha kupulumutsidwa koma pokhapokha atakhulupirira mwa Iye monga Mulungu woonekera m'thupi komanso monga Mesiya wao wolonjezedwa uja, Yesu anawafotokozera

kuti Iye anali nao maumboni atatu pa umulungu wake, ndipo maumboni onsewa anali odziwika bwino kwambiri kwa anthuwa. Umboni woyambirira ndi wa Yohane mbatizi, wachiwiri ndiwo ntchito zozizwitsa zimene Yesu anachita, ndipo umboni wachitatu ndi malemba oyera. Koma ngakhale panali maumboni amenewa, kumirira pa kusakhulupirira kwao kunam'pangitsa Yesu kunena mau pa ndime 40 akuti: “Ndipo simufuna kudza kwa Ine kuti mukhale nao moyo.”

Ha! Mau a tsoka lalikulu awa! Mwa mauwa Yesu anatsimikiza momveka kuti moyo umapezeka mwa Iye yekha, komanso kuti munthu angaupeze pa kungobwera kwa Iye. Yesu sanali kunena za moyo wathupi kapena kubwera kwathupi, pakuti amene anali kumumva Yesu anabwera kale pafupi ndi Iye mu thupi, koma Yesu anali kunena kubwera kwa uzimu ndi moyo wosatha umene umalandiridwa mwa kulumikizana ndi Iye kupyolera m'chikhulupiriro. Koma amene anali kumumvawa anakana kuchita chinthu chimodzicho chofunikira kukhala ndi moyo wosatha chifukwa anakana kum'khulupirira. Ndipo mau a Yesu awa akusonyeza kuti ali kuwatsutsabe iwo onse amene aumitsa mitima yao posafuna kubwera kwa Iye.

Kodi chinawaletsa ndi chiyani anthu achipembedzo chapanja pokhawa kubwera kwa Khristu? Kodi chikukuletsa ndi chiyani iwe, bwenzi langa wosapulumutsidwa'we, kudza kwa Khristu lero? Pamene ndiri kuika mfundo zazikulu zinayi za zifukwa zomwe ena samabwera kwa Yesu, ndiyembekeza kukuonetsa iwe kuti chifukwa chiri chonse chimene ndapereka ndi chosawiringulika. Ndifuna kukudandaulira iwe kuti, chonde! usiye zifukwazo ndi kubwera kwa Yesu Khristu!

## **1. Chifukwa choyamba ndi kuti simukudziwa kuti mukusowa Khristu kwambiri m'moyo mwanu.**

Anthu ena sabwera kwa Yesu chifukwa ali osadziwa chosowa chao monga ochimwa. Afarisi a panthawi ya Yesu ndi zitsanzo za padera pa umbuli umenewu. Pa Luka 18 Yesu anawaphera fanizo limene linawaloza onyenga awa amene “anadzikhulupirira mwa iwo okha kuti ali olungama” (Luka 18:9). Pamene alembi ndi afarisi anang'ung'udza zakuti Yesu alinkudya ndi kumwa pamodzi ndi amisonkho ndi ochimwa, Yesu anawayang'ana, nanena kuti, “Amene ali olimba safuna sing'anga; koma akudwala ndiwo. Sindinadza Ine kuitana olungama, koma ochimwa kuti atembenuke mtima” (Luka 5:31-32).

Chimene chinali choona kwa Afarisi mu zaka zikwi ziwiri zapitazo ndi choonanso lero kwa anthu ambiri: sadziwa ndi pang'ono pomwe kuti ali odwala. Sazindikira kuti ali ndi matenda a uzimu m'moyo mwao. Sapita kwa Sing'anga Wamkulu wa mioyo yao chifukwa sazindikira kuti ali ndi vuto. Koma kuganiza molakwa choncho pa vuto lenileni la moyo wako ndi kosawiringulika, simungathe kuwiringula chifukwa cha umboni wapoyera **wa m'Bukhu Lopatulika** ndi **chikumbumtima chanu**.

### *a. Umboni wam'Baibulo.*

Tawerengani bukhu liri lonse la m'Baibulo, ndipo mudzawerenga za makhalidwe auchimo a anthu. Kuchokera pa mbiri ya Adamu ndi Hava, pakusamvera Mulungu, kufikira ku mbiri yonse ya anthu onse m'Baibulo, Mau a Mulungu akutionetsera kuti ndife mtundu wochimwa ndi wodetsedwa. Koma ngati mudziganzira nokha kuti siziri kukukhudzani, ganizirani malemba a mtumwi Paulo, kunena m'malo mwa Yesu Khristu ndi motsogozedwa ndi Mzimu Woyera: “Mwa Adamu onse amwalira” (1 Akor. 15:22), kapena pa Aroma 5:12, kuti “Chifukwa chake, monga

uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi, ndi imfa mwa uchimo; chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa.”

Zoonadi, tiri ochimwa chifukwa cha uchimo wa chibadwa ichi. Paulo akufotokoza za ife monga “ana amkwiyo chibadwire” (Aefeso 2:3). Davide, amene ali munthu wa pa mtima wa Mulungu, anadzichitira umboni kuti, “Onani, ndinabadwa m'mphulupulu; ndipo mayi wanga anandilandira m'zoipa (Masalmo 51:5). Aliyense wa ife talandirana nacho chibadwa cha uchimochi, ndipo kuchimwa kumabwera mwa chibadwa kwa ali yense wa ife. Tiri ochimwa chifukwa chakuswa malamulo a Mulungu olembedwa m'mitima yathu mu Mau a Mulungu. “Tonse tasochera ngati nkhosha; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse (Yesaya 53:6). Paulo nayenso anenetsa apa ndi ulamuliro wotheratu kuti, “Palibe m'modzi wolungama, inde palibe m'modzi” (Aroma 3:10).

### *b. Umboni wa chikumbumtima chanu.*

Umboni wochokera m'malembo si wokhawo; palinso umboni wam'kati wa chikumbumtima chanuchanu. Chikumbumtima ndi chochitachita mwa munthu ali yense, kapena pakuneneza zochita munthu zoipa kapena kutama izo zimene zili zabwino (Aroma 2:15). Mumadziwa kuti chikumbumtima chimapangitsa kuti tchimo lisakome, ndipo chifukwa chake munthu amapezerapo njira zotsutsana nacho. Kukanakhala kuti chikumbumtima chinalankhula momveka, chikanafuula momveka m'mene mtima wanu waipira. Chikanaulula zokhumba zonse ndi zilakolako zonse zoipa zokhala mu mzimu wanu. Kukanakhala kotheka kuti inuyo mumvetsere chikumbumtima chanu simukanatha kukhala wosadziwa zakuti mukusowa Yesu Khristu. Inuyo mulikudziwa kuti muli pansu pa chiweruzo cha Mulungu chifukwa cha tchimo lanu, ndi kudziunjikira

zotsatira za chilango cha uchimocho. Komanso mukudziwa kuti inu mwa inu nokha mulibe mphamvu ya kudzithandiza nokha.

Kodi ndi angati amene amanyozera umboni wa Baibulo ndi kulimbana ndi umboni wa chikumbumtima chaochao! Musanyoze uthenga wa chifundo chaulere cha Khristu! M'malo mwake, pempherani kuti mukathe kuzindikira kusowa kwanu kwakukulu komanso kukula kwa mlandu ndi kuipa kwanu pamaso pa Mulungu. M'malo mokhala ngati Mfarisi uja wa pa Luka 18 amene anaima monyada pamaso pa Mulungu ndi kudzitamandira pa ubwino wake, iwe tsopano udziweramitse pansi modzichepetsa monga wamsonkho uja ndi kupfuula kuti, "Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa."

## **2. Chifukwa chachiwiri chingakhale kuti simulapa pamene Yesu ali kukutsutsani ndi mau ake.**

Mwina mwake muli okonzeka kuvomera kusowa kwanu ndi kuthawa mtsutso ndi chilango zimene ziri m'chikumbumtima chanu, koma pali chifukwa china chimene chimakupangitsani kuti musabwere kwa Yesu. Mwina mwake simulapa kapena kukhala ndi mtima wachisoni pamene Khristu ali kukutsutsani.

Pamene Yesu aitana kuti mubwere kwa Iye chimakhalanso lamulo lakuti inu musiyeye machimo anu. Mngelo anauza Yosefe kuti, "Udzamutcha dzina lake Yesu, chifukwa adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo" (Mat. 1:21). Sadzawapulumutsa ndi kuwasungabe m'machimo mwao, koma adzawapulumutsa **kuchokera ku machimo ao**. Yesu ananena pa Luka 5:32 kuti, "Ndadza kuitana ochimwa kuti atembenuke mtima." Njira zakuti inu mukwatidwe ndi Yesu, ndi njira yakuti inu mulekane kotheratu ndi machimo anu. Simungathe kulekanitsa kulapa ndi chikhulupiriro ndi chikhululukiro. Paulo anatsimikiza kuti Uthenga

Wabwino weniweni wa Yesu Khristu ndi “kulapa kwa Mulungu ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Ambuye wathu Yesu Khristu” (Machitidwe 20:21). Petro anauza Ayuda pa Machitidwe 5:31 kuti Mulungu anakweza Yesu kukhala Kalonga ndi Mpulumutsi kuti “apatse kwa Aisrayeli kulapa ndi chikhululukiro cha machimo.”

Kapena vuto lanu silingakhale kusakhudzidwa. Zoonu mungazindikire mwachisoni za kusowa kwanu kwakukulu kwa chikhululukiro ndi mtendere. Koma simuli okonzeka kusiya machimo anu ndi kubwera kwa Khristu pakumvera Mau ake. Limeneli linali vuto la mwini chuma pa Mateyu 19. Moona mtima iye analakalaka moyo wosatha ndipo poufunafuna anadza kwa Yesu. Koma Yesu, pokhala ndi nzeru zakudziwa zonse mwa munthu, anatchula chinthu chimodzi – chikondi cha munthuyu cha pa chuma. Yesu anayenera kukhala Mbuye wake yekhayo, ndipo anati, “pita, kagulitse zonse uli nazo, nupatse aumphawi, ndipo udzakhala ndi chuma kumwamba ndipo ukadze kuno unditsate.” Koma mnyamata mwini chumayo sanalole kugonjera lamulo la Yesu lija, ndipo mau anena kuti, “anamuka wa chisoni.”

Sitiyenera kumaganiza kuti nkhani apa ndi lamulo loti aliyense asiye chuma ayi, pakuti Yesu anaitanapo anthu angapo achuma monga Mateyu ndi Zakeyu, ndipo Yesu sanatchulepo za chuma chao cha anthuwa. Koma pamene anachita ndi wochimwa wina aliyense, monga mkazi wa kuSamariya pa Yohane 4, Yesu anapeza tchimo la munthuyo ndipo molimba mtima anadzudzulapo. Yesu akunena kwa ali yense wa ife kuti moyo wosatha uyenera kupezeka mwa Yesu yekha pamene tigwirizana kotheratu ndi Iye yekhayo. Pa Mateyu 6:24, akuti, “Simungathe kukhala kapolo wa Mulungu ndi wa chuma.” “Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wake, nanditsate Ine,” (Marko 8:34). Kodi mwaona kuti

kusalapa pamene Mau a Yesu amakutsutsani ndi chinthu chimene simungathe kuwiringula? Ambuye Woyera, wangwiro wa ulemerero akukuitanani kuti muchoke m'machimo anu, kuti akupatseni moyo wosatha, ndipo inu mumakana kuwasiya machimowo. Koma machimo amene muli kuwakakamira'wo, kodi adzakuchitirani chiyani ku mathero a zonse? "Mphotho yake yauchimo ndi imfa," akutero Mtumwi Paulo pa Aroma 6:23. Chipulumutso kupyolera mwa Yesu Khristu chinapatsidwa kuti chikuomboleni ku chilango ndi mphamvu za tchimo. Chinapatsidwanso kukuchotserani machitidwe ndi maonekedwe onse a uchimo, adalitsike Mulungu! Kodi muumirirabe ku machimo anu amene adzangokukokerani ku Gehena?

Yesu akudziwa kuti kulekana ndi tchimo kumakhala ngati kopweteka kwa ife. Anakamba za machimo monga diso lokondeka la kumanja kapena ngati dzanja lokondeka la kumanja. Yesu akudziwa bwinobwino kuti kulapa kwenikweni, kuvomereza kwenikweni ndi kusiya tchimo, kungabweretse kukhumudwa, kusamvana ndi anzathu, kutaya chuma ndi ululu wakulekana ndi okondeka athu. Pamene Yesu ananena kwa Ayudawo, "Simubwera kwa ine," anadziwa kuti anthuwa amakonda kulemekezeka nawo ulemu wochokera kwa anzao (Yoh. 5:44). Chifukwa cha mitima yao yonyadayo, sanathe kutsatira Mphunzitsi wonyozekayu. Yesu anadziwa kunyinyirika kwao, koma sanachepetsere konse mau ake okaniza thupi.

Kodi mwaona kuti kusalapa uku sikungokhala kokha kosawiringulika komanso kopanda nzeru? Taganizirani za m'mene moyo umaipira umene ndi wolowerera m'tchimo. Tayang'anani mosamalitsa pa moyo wopunduka wa iwo amene anakaniza kuvomera chisomo cha Mulungu pamene anali ana—anthu amenenso okhaokhawa akhala chikwaniritso cha ulosi wa Mulungu mu Yesaya, "Koma oipa ali ofanana ndi

nyanja yowinduka; pakuti siingapume, ndi madzi ake autsa matope ndi uve. Palibe mtendere, ati Mulungu wanga, kwa oipa” (Yesaya 57:20-21). “Koma njira ya achiwembu iri makolokoto” (Miyambo 13:15). Taonani mantha amene amadzaza pa imfa ya iwo amene amafa m’machimo ao. Taonani Tsiku la Chiweruziro limene likubwera, pamene anthu otchuka a pa dziko la pansi adzalirira mapiri ndi matanthwe kuti awagwere, kuti awabise ku “mkwiyo wa Mwanawankhosa” (Chivumbulutso 6:16). Taonani mu Gehena mwenimwenimo m’mene anthu osalapa alikuponyedwa mu ng’anjo ya moto; “kumene kudzakhala kulira ndi kukukuta mano” (Mat. 13:42). “Ndipo utsi wa kuzunza kwao ukwera ku nthawi za nthawi” (Chivumbulutso 14:11).

Kotsiriza yang’anani pamtanda. Taonani Mbuye waulemerero, Munthu yekhayo amene anakhala moyo wopanda uchimo, amene pamtanda anayesedwa wochimwa chifukwa cha anthu ake. Tayang’anani mtengo wa malipiro umene Yesu anapereka chifukwa cha machimo amene inu mukonda. Taonani mazunzo ake m’manja a anthu oipa. Ganizirani ululu waukulu wosasimbika womwe anamva pamene mkwiyo wa Atate ake unathiridwa pa Iye chifukwa cha tchimo la munthu. Talingilirani zimenezi mpaka mutatha kunena limodzi ndi John Newton kuti:

*“Mpulumutsi wakukha mwazi ndamuona,  
ndipo tsopano ndidana nalo tchimo langa.”*

Ngati kuganiza uku sikuli kokwanira kukuchotsani ku machimo amenewa amene tsopano akuoneka ngati okondeka kwambiri kwa inu, chidzakhala cholungama kwa Mulungu pa tsiku lalikululo kunena kwa inu, “Chokani kwa Ine, otembereredwa inu” (Mat. 25:41). “Efraimu waphatikana ndi mafano, mlekeni”(Hoseya 4:17). Musamiriremirirebe mu Gehena kukangamira ku machimo anu amene mumawakondawo. Bwerani kwa Yesu pakuitana kwake, kuti mukhale ndi moyo.

### 3. Chifukwa chachitatu chingakhale chakuti simukhulupirira malonjezo a Yesu.

Mwina mwake uchimo wanu si woti mukumakakamira molimba mtima machimo ooneka ngati oopsya. Kapena mwasiya kale machimo ambiri, chifukwa cha inu nokha kapena chifukwa chofuna kuchitira ulemu anthu ena. Koma lilipo tchimo limodzi lobisika limene simunaliganizire chiyambire. Mwina mungaganize kuti si lalikulu kwambiri, kapena kuti si lopangitsa manyazi ayi. Tchimo limeneli ndi **kusakhulupirira malonjezo a Yesu.**

Koma mukuti, “Kusakhulupirira? Kodi ndi tchimo la mtundu wanji limeneli? Nanga Mulungu angandiimbe mlandu bwanji pa kusakhulupirira kanthu kena?” Mnzanga, taganiza kwa kanthawi m’mene kusakhulupirira kungathe kukhala chimodzi cha zopinga zokulepheretsani inu kubwera kwa Khristu, kotero kuti inu n’kulephera kulowa ku Paladizo!

Malonjezo onse a Yesu ndi omveka, otsimikizika komanso a kwa anthu onse. Tawerengani zitsanzo za malonjezo ake zili m’munsizi. Tapezani mavesi ake m’Baibulo kuti mudzionere nokha kuti malonjezo amenewa ndi a ulere kwathunthu osafunanso inu kuti muyambe mwachitapo kanthu kapena kukwaniritsa zokuyenerezani ayi.

Mateyu 11:28 “Idzani kuno kwa Ine **nonsenu** akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu.”

Aroma 10:12 “Pakuti Yemweyo ali Ambuye wa **onse**, nawachitira zolemera **onse** amene aitana pa Iye.”

Aroma 10:13 “Pakuti amene **ali yense** adzaitana pa Dzina la Ambuye adzapulumuka.”

Yohane 5:24 “Iye wakumva Mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao

moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wachokera ku imfa, nalowa m'moyo.”

Yohane 6:37 “Wakudza kwa Ine sindidzam'taya kunja.” (Yesu sadzam'taya kunja ***konse.***)

Mulungu anafanizira ntchito yake yachipulumutso ndi phwando la ukwati, nati, “zinthu zonse zapsya, idzani kuukwati” (Mateyu 22:4). Mulungu wakonza zonse, ndipo Mulungu wachita zonse zoyenera kuchitika. Sitifunika kutenga kanthu popita, koma kungobwera basi.

Popeza kuti tili nawo malonjezo osafuna zoyenereza za chikhululukiro ndi kulandiridwa, kodi muli kuonapo kuti tchimo losakhulupirira ndi losawiringulika? Phwando la Uthenga Wabwino lalengezedwa kale ndipo Mulungu watuma kale antchito ake kunena, “Bwerani, pakuti zonse zatha kukonzeka” (Luka 14:17). Kodi mumadikirirabe panja pa nyumba ya phwando, wotaika ndi wotsutsidwa chifukwa mwakana mwa kusakhulupirira kwanu, kukana kulandira chifundo cholonjezedwa cha Mulungu? Mwina mukudziwa kusowa kwanu kwenikweni; mukudziwanso kusalapa kwanu pa machimo anu, koma simulola kukhulupirira umboni wa Mulungu wonena za kukwanira kwa Mwana wake monga Mombolo kwa anthu ochimwa—Mulungu amene anakamba momveka kuchokera Kumwamba, “Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, mverani Iye” (Marko 9:7).

Kudzakhala mitundu yosiyanasiyana ya anthu ochimwa ku Paladizo. Kudzakhala ochimwa oipitsitsa monga mkazi wochimwa wa pa Luka 7 amene mbiri yake imadziwika ndi onse. Kudzakhala ochimwa opanda chiyembekezo monga mbala imene umbala wake unayenera kupachikidwa. Kudzakhala anthu akupha ndi onyoza Mulungu Kumwamba monga Saulo wa ku Tariso ndiponso ngakhale anthu ena amene manja ao anapha

Mwana wa Mulungu (Machitidwe 2:23). Koma kudzakhala mtundu umodzi wa ochimwa, amene adzaonekeratu kuti **kulibeko**: kumeneko sikudzakhala **osakhulupirira**. Sikudzakhala anthu m'Mwamba amene sanalumikizane ndi Yesu Khristu m'moyo uno mwa chikhulupiriro.

Bukhu la Chivumbulutso limasonyeza zithunzithunzi zambiri za chiweruzo chotsiriza cha anthu. Zina za zifanizozi ziri zozizwitsa ndi zosamveka bwino, koma tayang'anani pa chithunzi chimodzi chooneka bwino cha amene ali kuima panja pa zipata za Kumwamba. Chivumbulutso 21:8 akuti, "Koma amantha, ndi **osakhulupirira**, ndi onyasa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi olambira mafano, ndi onse amabodza, cholandira chao chidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure; ndiyo imfa yachiwiri." Iwo amene miyoyo yao ndi yaulemu ndi yoongoka, koma itamatiridwa ndi kusakhulupirira adzatenga nao malo ao amuyaya pamodzi ndi iwo amene miyoyo yao inaonekera kuti ndi akupha, abodza ndi machimo ena aakulu.

Anthu'fe timaona ngati kusakhulupirira ndi kusakwanira kwa kanthu kena kapena ngati kanthu kena koperewera m'mtima kamene kamatisiya ife ofooka mu uzimu koma osati kuipiratu. Mulungu amaona kusakhulupirira monga kulili kwenikweni. Pamene Yesu ali kufotokozerwa za cholinga cha Mzimu Woyera pakubwera kudzatsutsa dziko lapansi chifukwa cha tchimo, panotu pali tchimo lalikulu limene Iye amaliunikira: "Chifukwa sakhulupirira Ine" (Yohane 16:9).

Ngati kufikira tsopano mwakhala osakhulupirira, kodi mungathe kusiya tchimo ili ndi kumamatira mwa chikhulupiriro kwa Khristu? Kodi mudzakhulupirira malonjezo ake ochuluka a chipulumutso, chikhululukiro ndi mpumulo?

#### **4. Chifukwa chachinayi chingakhale chakuti mukuyembekeza kuti mudzalandira bvumbulutso loonjezera kuchokera kwa Khristu.**

Kapena mpaka pano sitinasanthule chifukwa chanu chimene chikupangitsani kuti musabwere kwa Yesu. Mukuzindikira mkati mwanu chosowa chanu komanso inu muli okonzeka kusiya machimo anu. Muli kufunafuna kuika chikhulupiriro chanu mwa Yesu pa nthawi yoyenera, **koma mukufuna Mau oonjezera a kwa iwe wekha kuchokera kwa Iye.**

M'mene mumawerenga Baibulo, kaya kupyolera kuti mumawerenga nokha, kapena kuliphunzira pa banja, kapena kuti mumapita ku tchalitchi, izi zakuphunzitsani chinthu chofunika. Chimenecho ndi chakuti inu mudziwa kuti ngati simuli m'modzi wa anthu osankhidwa ndi Mulungu, simungathe kubwera kwa Khristu. Mukudziwa kuti Mulungu amadzutsa kaye wochimwa kuti azindikire chosowa chake. Mulungu am'koke ndipo am'patse mphatso ya chikhulupiriro. Ndipo mumayamba kuganizira, "Ndidziwe kaye kuti ndine wosankhidwa wake wa Mulungu, apo ayi, chikanakhala chopanda ntchito kwa ine kubwera kwa Khristu."

Chifukwa cha maganizo amenewa, mwina mwake inuyo mwatsimikiza kuti simungachitepo kanthu kufikira bvumbulutso lina libwera kuchokera kwa Khristu, lokuvumbulutsirani kuti ndithudi ndinu wake wa Mulungu. Sikuti mukanapempha kuti muone masomphenya kapena kumva mau usiku, koma mwina muli kuyembekeza kuti kapena vesi lapadera lidzakufikirani m'maganizo anu mwamphamvu, kapena kuti Mulungu adzakutsimikizirani munjira yapadera kuti ali nanu pompano, kapena kuti mudzapeza umboni wina wake wakutsimikiza zizindikilo za kubadwanso mwatsopano m'moyo wanu. Ndipo choncho, simudzabwera kwa Yesu Khristu chifukwa muli

kuyembekezera uthenga kapena vumbulutso kuchokera kwa Mulungu.

Ndi chifukwa ninji sichiri chofunikira kuyembekezera vumbulutso loonjezeralo? Ndime ya pa Yohane 5 ikutipatsa ife yankho lofunika ku funso limenelo. Yesu ananenetsa kwa Ayuda, kuti Chipangano Chakale chinayenera kukhala chitsimikizo chokwanira pa zonena zake. Pa 39 anati, “Musanthula m’malembo, popeza muyesa kuti momwemo muli nao moyo wosatha; ndipo akundichitira Ine umboni ndi iwo omwewo.” Pa vesi 46 Iye akuti, “Pakuti mukadakhulupirira Mose, mukadakhulupirira Ine; pakuti iyeyu analemba za Ine.” Tingathe kunenanso kuti Yesu akunena kuti, “Zimene Mau a Mulungu akunenera za Ine, kuchokera ku zolemba zakale za Mose kufikira mau otsiriza a aneneri otsiriza, ndi zokwanira kuti mutha kudza kwa Ine. Musayembekezere kanthu kena; mau awa ndi okwanira.”

Mau onenedwa kwa mwini chuma mu Gehena, ali kutsimikizanso chiphunzitso cha Yesu pa kukwanira kwa umboni wa malembo. Pa dandaulo la mwini chuma uja lakuti wina apite akachenjeze abale ake za mazunzo a m’Gehena, Abrahamu anayankha, “Ali ndi Mose ndi aneneri, amvere iwowo” (Luka 16:29). Komabe wachuma uja, anali ndi njira ina yomwe amaiona ngati yabwino koposa. “Iyai, atate Abrahamu, komatu ngati wina akapita kwa iwo wochokera kwa akufa adzasandulika mtima” (ndime 30). Tamvani mau a Yesu akulankhula pa yankho lotsiriza la Abrahamu: “Ngati samvera Mose ndi aneneri, sadzakopeka mtima ngakhale wina atauka kwa akufa.”

Kodi muli kuyembekezera bvumbulutso lina lirilonse lapadera lochokera kwa Mulungu kuti mutalandira limenelo mudzabwera kwa Yesu? Kodi muli kukaniza uthenga wa “Mose ndi aneneri” umene muli nao mu Baibulo lanu? Kodi muli kuona kuti

kuyembekezera kumeneko si kwa bwino? Musaganize kuti mchitidwe wanuwo ndi kuti muli kudzichepetsa pamaso pa Mulungu. Kudikirira kwanu kuli kuonetsa kunyada ndi kudzikuzza kwanu pamaso pa Mulungu, kukhala ngati muli kumuuzza Iye njira yomwe ayenera kuyendetsera chipulumutso chake. Ziri kuonetsa ngati kuti muli kumuuzza Mulungu kuti, “Mulungu, ndiri ndi njira yabwino ya chipulumutso yoposa njira zanu. Ndiri ndi njira ya padera yondiitanira, ndipo ndiri kuyembekeza bvumbulutso lapadera ili.” Choonadi ndi chakuti chikonzero cha chipulumutso cha Mulungu chinalembedwa momveka bwino kwa inu mu umboni wa Mau a Mulungu. Phwando laukwati la Uthenga Wabwino lakonzedwa, ndipo Mulungu ali kukuitanani kuti mukhale ndi moyo wosatha. Chokhacho chimene mungathe kuchita ndi kubwera.

Kodi Yesu Khristu ali kukuitanani? Kodi muli kudziona nokha osati ngati munthu wapadera, koma monga wosowa, wotaika, wochimwa woyenera Gehena? Tsono, tabwerani kwa Iye molapa ndi m'chikhulupiriro. Mumuone Yesu monga bwenzi loyenera, langwiwo la anthu ochimwa. Onani m'mene moyo wake wachilungamo ndi wangwiwo umakwaniritsira zoyeneretsa za lamulo la Mulungu. Ganizirani m'mene imfa yake inalowa m'malo mwathu kukwaniritsa kotheratu chilungamo cha Mulungu pa machimo athu. Musasokoneze zimene Mulungu wakonza, zosabvuta kukhala zobvuta, ayi, ingobwerani!

Mubwere kwa Khristu chifukwa cha mau olamulira, a chisomo, a Mulungu: “Ndipo lamulo lake ndi ili, kuti tikhulupirire Dzina la Mwana wake Yesu Khristu” (1 Yohane 3:23). Idzani kwa Khristu chifukwa cha lonjezo lachisomo la Mulungu; “Yense wakukhulupirira Iye, asatayike koma akhale nawo moyo wosatha” (Yohane 3:16). Lero, siyani zifukwa zirizonse zimene

zimakuletsani. Bwerani kwa Khristu, kuti mukhale ndi moyo. ✨